

Mulungu Anatumiza Mose ku Iguputo

EKISODO CHAPUTALA 3 MPAKA 12



MOSE!

YEHOVA ANAITANA MOSE
KUDZERA MWA MNGELO.

MOSE!

NDILI
PANO.

NDINE **MULUNGU** WA MAKOLO
AKO. ANTHU ANGA, AISIRAEI
AMENE ALI KU IGUPUTO
AKUZUNZIKA. NDIKUFUNA KUTI
UKALANKHULE NDI FARAO.
UKATULUTSE ANTHU ANGA
KU IGUPUTO.


MOSE NDI M'BALE WAKE ARONI, ANAPITA
KWA FARAO.

YEHOVA AKUTI:
"LOLANI ANTHU ANGA
APITE M'CHIPULULU
KUTI AKANDITUMIKIRE."

YEHOVA NDANI?
SINDILOLA KUTI
AISIRAEI APITE.

ARONI MPAKA ANACHITA **CHOZIZWITSA** KUTI FARAO ADZIWE KUTI
MULUNGU NDI AMENE ANAWATUMA. (ONANI EKISODO 7:8-13.)

KOMA FARAO **ANAUMITSA MTIMA WAKE.**
IYE SANALOLE AISIRAEI KUTI APITE.



KENAKO YEHOVA
ANABWERETSA **MILIRI 9** KWA
ANTHU A KU IGUPUTO.

MADZI A MUMTSINJE WA NAILO
ANASANDUKA **MAGAZI**.

ACHULE ANALI MBWEE
M'DZIKO LONSE LA IGUPUTO.

NTCHENTCHE
ZAMBIRIMBIRI **ZOLUMA**
ZINAYAMBA KUVUTITSA
ANTHU NDI NYAMA.

KENAKO PANABWERA **TIZILOMBO**
TINA TOULUKA **TOYAMWA** MAGAZI
NDIPO TINALI PALIPONSE.

MATENDA OSIYANASIYANA ANAPHA
NYAMA ZAMBIRIMBIRI.

AIGUPUTO NDI NYAMA ZAWO ANATULUKA
ZITHUPSA **ZOPWETEK**A KWAMBIRI.

MATALALA NDI MOTO ZINAONONGA MINDA
KOMANSO ZINAPHA ANTHU NDI NYAMA.

DZOMBE LINADYA CHOMERA
CHILICHONSE CHIMENE **MATALALA**
SANAWONONGE.

M'DZIKO LONSE LA IGUPUTO
MUNACHITA **MDIMA** WANDIWEYANI
KWA MASIKU ATATU.

KOMA FARAO **SANALOLE** KUTI
AISIRAEALI ACHOKE.

MOSE NDI ARONI ANAPITA
KWA FARAO **KACHIWIRI**.

YEHOVA WANENA KUTI:
“NDIBWERETSA **MLIRI**
WOMALIZA MU IGUPUTO.
PAKATI PA USIKU, MWANA
ALYENSE WOYAMBA
KUBADWA AMWALIRA.”

ZIMENEZI ZINACHITIKADI. USIKU UMENEWO, YEHOVA
ANATUMIZA MNGELO WAKE NDIPO ANAPHA **MWANA**
WAMWAMUNA WOYAMBA KUBADWA, M'BANJA
LILILONSE LA AIGUPUTO LOSAMVERA MULUNGU . . .

KUPHATIKIZAPO **MWANA**
WAMWAMUNA WA FARAO.
(ONANI SALIMO 78:49-51.)

PITANI,
KATUMIKIRENI
YEHOVA, MONGA
MOMWE
MWANENERA.

TSOPANO AISIRAEI ONSE ANALOLEDWA
KUCHOKA KU IGUPUTO.

KOMA SIKUTI FARAO ANAWASIYIRA POMWEPA.
KODI YEHOVA **ANAWATETEZA** BWANJI? MUDZAPEZA
YANKHO LA FUNSO LIMENELI M'NKHANI YOTSATIRA.

KODI TIKUPHUNZIRA CHIYANI PA NKHANIYI?

N'CHIFUKWA CHIYANI FARAO **SANAMVERE** MOSE
NDI ARONI?

ZOKUTHANDIZANI: EKISODO 9:17; SALIMO 66:
6, 7.

KODI MOSE ANALI **WOSIYANA** BWANJI NDI FARAO?
ZOKUTHANDIZANI: NUMERI 12:3.

MUKUGANIZA KUTI N'CHIFUKWA CHIYANI NDI
BWINO KUKHALA **WOFATSA** NDIPONSO WODEKHA
M'MALO MOKHALA WODZIKONDA KOMANSO
WOMVA ZAKO ZOKHA?

ZOKUTHANDIZANI: SALIMO 37:11; ZEKARIYA 7:
8-12.